15. Munthu wa nzeru ndi amene amamvera mawu a Khristu.

Kodi wofanana ndi munthu wopusa ndani amene anamanga nyumba yake pa mchenga?

______________________________

========================================================================

16. Munthu wopusa ndi amene samvera mawu a Khristu. Anthu anadabwa pamene Yesu anaphunzitsa m'njira yotere.

Mateyu 7:28-29:
> Ndipo panakhala pamene Yesu anatha mawu amenewa, makamu a anthu anazizwa ndi chiphunzitso chake: pakuti anawaphunzitsa monga mwini mphamvu, wosanga alembi awo.

Kodi mukuganiza kuti anthu amumpingo mwanu ali kuphunzira kumanga pa thanthwe?

______________________________

Kodi mukuganiza kuti ali kufunika thandizo lochokera kwa inu m'njira yotani?

______________________________

========================================================================

17. Tidzakambirana za yankho lanu m'kalasi.

Kodi Yesu anati munthu wanzeru ndi ofanana ndi yani amene anamanga nyumba yake pa thanthwe?

______________________________

______________________________

Kodi ndi ndani ali wofanana ndi wopusa amene anamanga nyumba yake pa mchenga?

______________________________

______________________________

========================================================================

SABATA LACHISANU NDI CHITATU: KHRISTU APHUNZITSA ZINA ZAMBIRI PA PHIRI
TSIKU LACHISANU: YOHANE ABWERETSA MAKAIKO AKE KWA YESU KUBWEREZA

1. Taona kuti Yesu anaphunzitsa ndi mphamvu. Anthu anadabwa ndi mawu ake.

Kodi Yesu anati munthu wanzeru ndi wofanana ndi yani amene anamanga nyumba yake pa thanthwe?

______________________________

______________________________

Kodi ndi ndani amene ali wofanana ndi munthu woposa amene anamanga nyumba yake pa mchenga?

______________________________

______________________________

==========================================================================

2. Munthu wanzeru ameneyu ndi amene amamvera mawu a Yesu. Munthu wopusa ndi amene samvera. Nthaŵi zina ife sitikhala wotsimikiza zoyenera kuchita. Nthaŵi zina ife timakhala ndi makaiko ngakhale kuti tatsata Yesu kwa nthaŵi yaitali. Yohane mbatizi anali ndi makaiko. Iye anali ndi mafunso. Iye anabwera nawo kwa Yesu. Chimenechi ndi chimene tiphunzire lero.

| |
|---|
| Pamene tibweretsa makaiko kwa Yesu monga Yohane Mbatizi anachitira Iye amaŵachotsa. |

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Luka 7:18-28. Pamene Yohane anali m'ndende, kodi iye anatsimikiza kuti Yesu anali wolonjezedwayo?

______________________________

==========================================================================

3. Iye anali ndi chitsimikizo. Herode chiwanga anaika Yohane m'ndende Herode anali munthu wochimwa ndipo Yohane anamudzudzula za tchimo lake. Kotero Herode anamuika iye M'ndende. Tsopano Yohane anali kumva za ulaliki wa Yesu. Iye sanathe kuona zomwe ali kuchita. Iye anatumiza ophunzira ena kuti akafunse Yesu.

Luka 7:19:

Ndipo Yohane anaitana aŵiri a ophunzira ake, naŵatuma kwa Ambuye, nanena, "Kodi ndinu wakudzayo, kapena tiyang'anire wina?"

Kodi ndani amene anali kukaika za Yesu pamene iye anali m'ndende?

___

====================================================================

4. Yohane Mbatizi anali ndi makaiko. Iye anaganiza kuti Yesu anali wolonjezedwayo, koma iye analibe chitsimikizo. Tikakhala Akhristu atsopano, mwina mumaganiza kuti simudzakhalanso ndi makaiko. Koma muli ndi njira zina zambiri zoyenera kuziphunzira zomwe Satana amagwirira ntchito Nthaŵi zonse iye amakangana ndi Mulungu. Iye amafuna kuchotsa chikhulupiriro chanu. Mulungu amakulolani kuti muyesedwe. Iye amadziŵa kuti ngati chikhulupiriro chathu chili choonadi mayesero adzachilimbikitsa.

Luka 7:20:

Ndipo pakufika kwa Iye anthu awo, Yohane Mbatizi watituma ife kwa Inu, kuti, kodi ndinu wakudzayo, kapena tiyang'anire wina?

Kodi Yohane anachita chiyani kuti achotse chikaiko chake?

___

====================================================================

5. Yohane anatumiza anthu kwa Yesu. Ife sitingathe kutumiza anthu kwa Yesu. Komà tikhoza kupereka chikaiko chathu m'mapemphero. Yesu anali njeza kuti ngati ife titafunitsitsa kudziŵa, Iye adzationetsa ife choonadi.

Yohane 7:17:

Ngati munthu aliyense afuna kuchita chifuniro chake, adzazindikira za chiphunzitsocho, ngati chichokera kwa Mulungu, kapena ndilankhula zochokera kwa Ine ndekha.

Ngati ife tikufuna kutsatira Yesu, kodi Iye adzatisiya tili ndi chikaiko kapena kuti adzatichotsera chikaikocho?

___

___

6. Iye adzatichotsera chikaiko chonse. Iye anachitira zimenezi Yohane Mbatizi. Yohane analalikira kuti Yesu adzaweruza anthu ochimwa. Koma Yohane poona kuti iye ali m'ndende, Herode akupitirira kuchitabe machimo anakaika. Iye anakaika ngati anali kulalikira za Yesu mwana wa Mulungu wolonjezedwayo. Pamene anthu a Yohane anabwera, Yesu anali kuchiza anthu ambiri.

Luka 7:22:

> Ndipo anayankha, nati kwa iwo, Mukani, muuze Yohane zimene mwaziona, nimwazimva; anthu akhungu alandira kuona kwawo, opunduka miyendo ayenda, akhate akonzedwa, ogontha akumva, akufa aukitsidwa, kwa aumphawi ulalikidwa Uthenga Wabwino.

Kodi ndi ndani anachotsa makaiko a Yohane Mbatizi? ____________________

===================================================================

7. Yesu mwini wake ndiye anachota zimenezi. Iye anadziŵa kuti ndikovuta kwa Yohane kuti amvetsetse njira yakagwiridwe kake ka ntchito. Motero Iye anaonjezera kanthu kena ku mawu ake.

Luka 7:23:

> Ndipo wodala iye amene sakhumudwa chifukwa cha Ine.

Yesu anatanthauza kuti munthu sayenera kuvutika chifukwa cha njira imene Yesu amagwirira ntchito. Nthaŵi zina Yesu anagwira ntchito pang'ono. Iye amagwira ntchito m'njira yosiyana ndi imene ife timaiganizira. Yesu anaonetsa kuti Yohane anadza kudzathandiza anthu komanso kudzaŵaweruza.

Pamene ife tibweretsa makaiko athu kwa Yesu monga Yohane Mbatizi anachitira, kodi Yesu amachita nawo chiyani?

________________________________

__________________________________________________________________

===================================================================

8. Iye anaŵachotsa mavutowo. Iye anamvetsetsa mavuto athu. Yesu anakonda Yohane. Anthu atangochoka, Yesu anayamba kulemekeza Yohane. Iye anadzudzula Afarisi chifukwa chosakhulupirira zonena za Yohane. Yesu anadzudzula Yohane chifukwa cha kukaika kwake. M'malo mwake Iye anachotsa makaiko ake. Patapita masiku Yohane anaphedwa ndi mfumu Herode. Iye anafa ali kudziŵa kuti wachita ntchito yake ndi kuti Khristu anabwera.

Ifenso tiyenera kubweretsa makaiko athu kwa Yesu. Kodi ife tikhoza kuchita zimenezi motani?

_______________________________

_______________________________________________

===========================================================

9. Tikhoza kubweretsa makaiko athu kwa Yesu mwa mapemphero. Akhristu ambiri ali ndi makaiko, koma Mulungu anafuna kuti ife tikhale ndi chikhulupiriro. Yesu anayenera kuphunzitsa akuphunzira ake za chimenechi.

Yohane 7:5:
Pakuti angakhale abale ake sanakhulupirire Iye.

Tsiku lina Yesu ndi akuphunzira anali kupita pa ngalawa. Mphepo ya mkuntho inadza. Iwo anali pangozi yomira m'nyanja. Ndipo akuphunzira anali kuchita mantha. Yesu analetsa mphepo nanena kuti, "Chikhulupiriro chanu chiri kuti?"

Pamene ife tibweretsa makaiko athu kwa Yesu monga momwe Yohane Mbatizi anachitira, kodi Yesu anachita chiyani ndi iwo?

_______________________

_______________________________________________

===========================================================

10. Iye amaŵachotsa makaikowo. Koma ngati ife sitibweretsa makaikoŵa kwa Yesu sangathe kuŵachotsa konse. Muli kukumbukira kuti m'mudzi mwawo momwe sanathe kuchita zozizwitsa zambiri. Pamene tikukaika za Iye, Yesu sangathe kutithandiza.

Patapita nthaŵi, Yesu anati zisoni zidzadza ku Yerusalemu ndi mizinda ina. Iwo anakana kulapa ndi kukhulupirira mwa Yesu. Ngati ife tikhalabe ndi makaiko kapena kuyesa kuŵabisa, ndiye kuti adzakula. Chimaliziro chake cha makaiko ndi kusakhulupirira ndicho chiweruzo.

Kodi inu mumayenera kubisa makaiko anu kapena kuŵabweretsa kwa Yesu?

_______________________________________

===========================================================

11. Muyenera kuŵabweretsa kwa Yesu.

Pamene tibweretsa makaiko athu kwa Yesu monga momwe Yohane Mbatizi anachitira, kodi Yesu amachita nawo chiyani? ________________________

________________________________________________________

========================================================

Sabata ino ndi sabata yatha taphunzira zinthu zambiri. Tsopano tiyeni titenge nthaŵi yobwereza maphunziro ameneŵa. Lembani yankho la funso lililonse. Tsopano bwererani ku phunziro kuti muone ngati mwalondola. Ngati mwalephera funso lililonse, lembani yankho lolondola pamwamba pa lamulo.

MAFUNSO OCHOKERA PA SABATA LACHISANU NDI CHIŴIRI:

1. Kuchokera m'chiphunzitso cha Yesu cha pa phiri, kodi ndi ndani amene ali odala chifukwa adzakhuta? ________________________

________________________________________________________

Ndani amene ali odala chifukwa adzaona Mulungu? ________________

________________________________________________________

Kodi ndani amene ali odala chifukwa uli wawo ufumu wakumwamba?

__________________________ __________________________

2. Kodi Yesu ananena zinthu ziŵiri zotani kuti Akhristu tiri monga chiyani m'dziko lapansi?

   (1) ______________________ (2) ____________________

3. Lembani Mateyu 5:16: ____________________________________

   ________________________________________________________

   ________________________________________________________

4. Ngati inu mwabwera kudzapembedza Mulungu ndi kukumbukira kanthu kena komwe mbale wanu anakulakwirani inu, kodi muyenera kuchita chiyani?

5. Ngati inu mutayang'ana kwa mkazi ndi kumkhumba iye m'njira yoipa, kodi Yesu anati muli kuchita chiyani?

6. Pa Mateyu 5, kodi Yesu ananena kuti sitiyenera kuchita chiyani kuti anthu akhulupirire mawu athu?

7. Mmalo mobwezera choipa kwa adani athu, kodi Yesu anati tiyenera kuchita chiyani kwa iwo?

(1)

(2)

8. Kuchokera pa Mateyu 6, kodi ndi kaperekedwe, ndi kapempheredwe ndi kasalidwe kotani kamene Mulungu angadzaperekere mphotho?

MAFUNSO OCHOKERA KU SABATA LACHISANU NDI CHITATU:

10. Kodi chimaoneka ndi chiyani ngati titamayesa kutumikira Mulungu ndi zinthu za dziko lapansi pa nthaŵi imodzi?

11. Lembani Mateyu 6:33:

12. Kuchokera pa Mateyu 7, kodi tiyenera poyamba kuchita chiyani pamene tikuweruza ena?

13. M'njira yomwe ife timaperekera zinthu kwa ana athu, kodi Mateyu 7 amanena kuti Mulungu adzatipatsa chiyani pamene ife tipempha?

14. Kuchokera m'chiphunzitso cha Yesu cha pa phiri, kodi ndi m'njira yotani imene tingaganizire za anthu ena?

______________________

______________________

15. Kodi Yesu anati ife tikhoza kuŵadziŵa bwanji aneneri onyenga?

______________________

16. Kodi Yesu anati munthu wa nzeru ndi wofanana ndiyani amene anamanga nyumba yake pa thanthwe?

______________________

Kodi ndi ndani amene ali wofanana ndi munthu wopusa amene anamanga nyumba yake pa mchenga?

______________________

______________________

17. Pamene mubweretsa makaiko anu kwa Yesu monga Yohane Mbatizi anachitira, kodi Yesu anachita nawo chiyani makaikowo?

______________________

Pamene mwadziŵa mayankho onse. Bwereraninso ku tsamba la sabata 6, tsiku la 4. Phimbani mayankho amene mwalemba. Yesani kuyankha mafunso onse. Ndipo pitani pa phunziro la sabata la 3 Tsiku 4. Bisani mayankho anu. Yesaninso kuyankha mafunso ameneŵa.

SABATA LACHISANU NDI CHINAYI: KHRISTU APHUNZITSA ANTHU AMBIRI
TSIKU LOYAMBA: KHRISTU M'NYUMBA YA SIMONI

1. Pa sabata zonse ziŵirizi taona mmene Yesu anaphunzitsira ophunzira ake. Nthaŵi zina Iye anali kuphunzitsa ophunzirawo pa okha. Pa nthaŵi zina Iye anali kuphunzitsa anthu onse. Yohane Mbatizinso anasoŵeka maphunziro.

Ngati ife tibweretsa makaiko athu kwa Yesu monga Yohane Mbatizi anachitira, kodi Yesu amachita nawo chiyani?

______________________________

==========================================================================

2. Yesu amatichotsera makaiko athu. Iye amatithandiza m'njira zina. Iye anathandiza Afarisi ndi mkazi wochimwitsitsa. Tsiku lina munthu wina wotchedwa Simoni anaitana Yesu kunyumba yake kuti akadye. Yesu anapita kunyumba kwa Simoni. Mkazi wochimwa koposa anadza m'nyumbamo. Chinthu china chodabwitsa chinaoneka. Chimenechi ndicho chimene tiphunzire lero.

(1) Kuchokera m'maphunziro a Yesu kwa Simoni ndi mkazi wochimwa kwambiriyu, ife tiyenera kukhala ndi chikhulupiriro pofuna kuti tikhululukidwe.

(2) Kukhala okhululukidwa kumaika chikondi m'mitima ya okhulupirira.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Luka 7:36 mpaka 50. Ŵerenganinso ndime 36. Kodi Simoni amene anapempha Yesu kukadya naye anali munthu wotani?

______________________________

==========================================================================

3. Simoni anali Mfarisi. Ambiri mwa Afarisi anadana ndi Yesu.

Luka 7:36:
Ndipo mmodzi wa Afarisi anamuitana Iye kuti akadye naye. Ndipo analoŵa mnyumba ya Mfarisi, naseyama pachakudya.

Simoni anaitana Yesu kuti akadye naye. Koma iye sanachite kwa Yesu monga momwe mulendo anayenera kulandiridwa. Nthaŵi zonse alendo anali kupatsidwa madzi kuti atsuke mapazi awo. Iwo anali kupatsidwa mafuta

Kodi mukuganiza kuti iye anali ndi chikhulupiriro mwa Yesu kuti akhoza kumukhululukira machimo?

______________________________________________

==========================================================================

4. Ine sindikukhulupirira kuti Simoni anali ndi chikhulupiriro mwa Yesu. Komanso mkazi wochimwa kwambiri analoŵa momwemo. Buku Lopatulika limanena kuti iye anali mkazi wa mumzindamo, koma wochimwa. Iye anayenera kuti anamva za Yesu kuti ali kulalikira. Tsopano anamva kuti Yesu ali mnyumba ya Simoni. Iye anadza mkatimo nadzoza Yesu ndi mafuta onunkhira kwambiri. Yesu anakhoza kuona zomwe zinali mkati mwa mtima wa mkazi ameneyu.

Yohane 2:25:

> Ndipo sanasoŵa wina achite umboni za munthu; pakuti anadziŵa Iye yekha chimene chinali mwa munthu.

Kodi muli kuganiza kuti mkazi ameneyu anali ndi chikhulupiriro cha mwa Yesu?

______________________________________

==========================================================================

5. Mkazi ameneyu anali ndi chikhulupiriro. Yesu anadziŵa kuti anatero. Iye anakhoza kuona mitima ya amuna ndi akazi. Iye ananena kuti chikhulupiriro chake ndicho chamupulumutsa iye.

Luka 7:38,48:

> Naimirira kumbuyo, pamapazi ake nalira, nayamba kukhathamitsa mapazi ake ndi misonzi, nawapukuta ndi tsitsi lamutu wake, nawapsopsonetsa mapazi ake, naŵadzoza ndi mafuta onunkhira bwino... Ndipo anati kwa mkazi machimo ako akhululukidwa.

Kodi mkaziyo anapeza chiyani chifukwa cha chikhulupiriro chake?

__________________________________________________________________________

==========================================================================

6. Machimo ake anakhululukidwa. Chikhulupiriro cha mwa Yesu chimabweretsa chikhululukiro cha machimo chifukwa Yesu ndi mpulumutsi. Simoni Mfarisi sanadziŵe zimenezi. Iye anakaika kuti Yesu ndi mneneri. Iye anali wodabwa kuti mkazi wochimwa m'moyo mwake amkhudze.

Luka 7:39:

Koma Mfarisi, amene adamuitana Iye, pakuona, ananena mwa yekha, nati, "Akadakhala mneneri uyu akadazindikira ali yani, ndi wotani mkaziyo womkhudza Iye, chifukwa ali wochimwa.

Mkaziyo anali wochimwa, koma kodi chomwe anali nacho ndi chiyani chimene Simoni analibe?

______________________________________________

==========================================================================

7. Mkazi anali ndi chikhulupiriro. Koma Yesu anali kuona chikaiko mumtima wa Simoni. Iye anauza Simoni kuti anali ndi kanthu konena kwa iye Chimene Yesu ananena ndi ichi.

Luka 7:41-43:

Munthu wokongoletsa ndalama anali nawo amangaŵa aŵiri; mmodziyo anali ndi mangawa ace a marupiya mazana asanu, koma mnzake makumi asanu. Popeza analibe chobwezera iwo, anaŵakhululukira onse aŵiri. Chotero, ndani wa iwo adzaposa kumkonda? Simoni anayankha, nati, Ndiyesa kuti, iye amene anamkhululukira zoposa. Ndipo anati kwa iye, "Waweruza bwino.

Taganizirani za nthano imene Yesu anainena. Kodi Yesu amachita chiyani kwa amene ali ndi chikhulupiriro?

______________________________

==========================================================================

8. Yesu amakhululukira machimo awo. Iye anakhululukira mkazi wochimwa. Yesu anakhoza kukhululukira machimo chifukwa Iye ndi Mpulumutsi wa dziko lapansi. Kaŵirikaŵiri Buku Lopatulika limanena za zimenezi. Ife tiyenera kukhulupirira.

Mateyu 1:21:

Udzamutcha dzina lake Yesu; pakuti Iyeyo adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo.

Yohane 1:29:

Onani mwana wa nkhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo lake la dziko lapansi.

Kodi ife tiyenera kukhala ndi chiyani kuti tikhale wokhululukidwa?

________________________________________________________________

================================================================

9. Ife tiyenera kukhala ndi chikhulupiriro. Tiyenera kukhala ndi chikhulupiriro cha mwa Yesu monga amene angapulumutse wina aliyense ku machimo. Yesu sanangobwera kudzalalikira kokha zotsutsa tchimo monga mneneri. Iye anabwera monga Mpulumutsi kwa onse amene ali ndi chikhulupiriro mwa Iye. Iye anabwera kudzachotsa katundu wa uchimo m'mitima mwathu. Iye anabwera kudzatsuka mitima yanu ndi kukupatsani chikondi.

Luka 7:48-50:

> Ndipo anati kwa mkazi, "Machimo ako akhululukidwa." Ndipo iwo akuseyama naye pa chakudya anayamba kunena mwa okha. "Uyu ndani amene akhululukiranso machimo?" Ndipo Iye anati kwa mkaziyo, "Chikhulupiriro chako chakupulumutsa iwe; muka ndi mtendere,"

Kodi inu muli ndi chikhulupiriro chakuti Yesu ndi Mpulumutsi wa dziko?

________________________________________

Kodi muli ndi chikhulupiriro chakuti Yesu anakhululukira machimo anu?

______________________________________________

================================================================

10. Ine ndiri wokondwa ngati mwatha kuyankha kuti inde ku mafunso onseŵa.

Kuchokera ku chiphunzitso cha Yesu kwa Simoni Mfarisi ndi mkazi wochimwayo, kodi ife tiyenera kukhala ndi chiyani kuti tikhululukidwe?

__________________________________________

================================================================

11. Ife tiyenera kukhala ndi chikhulupiriro. Yesu anaonetsa Simoni kuti amene amakhululukidwa zambiri ndi amene amakonda koposa.

Luka 44:46:

Ndipo mmene Iye anacheukira kwa mkaziyo, anati kwa Simoni, Upenya mkazi ameneyu kodi? Ndinaloŵa mnyumba yako, sunandipatsa madzi akusambitsa mapazi anga; koma uyu anakonkha mapazi anga ndi misonzi, naŵapukuta ndi tsitsi lake. Sunandipatsa mpsopsono wa chibwenzi, koma uyu sanaleka kupsopsonetsa mapazi anga, chilowere muno Ine. Sunadzoza mutu wanga ndi mafuta; koma uyu anadzoza mapazi anga ndi mafuta onunkhira bwino.

Simoni sanakonde Yesu kwambiri. Kodi iye anaonetsa zimenezi motani?

---

12. Iye sanampatse madzi Yesu. Iye sanamupatse mpsopsono. Iye sanampatse mafuta odzola. Zimenezi ndizo zimene anthu anali kuchita pa nthaŵi imeneyo kuonetsa kwa mlendo. Koma mkazi ananyowetsa mapazi ake a Yesu ndi misonzi. Iye anapsopsona mapazi ake. Anamudzoza ndi mafuta onunkhira kwambiri. Chimenechi ndi chimene Yesu ananena za mkaziyu.

Luka 7:47:

Chifukwa chake, ndinena kwa iwe, machimo ake, ndiwo ambiri, akhululukidwa; koma munthu anene anamkhululukira pang'ono, iye akonda pang'ono.

Pamene mkazi anachita zinthu zimenezi kwa Yesu, kodi iye anaonetsa chiyani?

---

13. Zinaonetsa kuti mkaziyu anakonda Yesu. Yesu anakhululukira iye machimo ambiri. Ife timakonda Yesu chifukwa Iye anatikhululukira machimo athu. Yesu anakonda mkazi amene anali wochimwa. Iye anakonda Simoni. Ndipo Iye amakukondani inu. Yesu anauza Simoni za angongole aŵiri.

Luka 7:42-43:

Popeza analibe chobwezera iwo, anawakhululukira onse aŵiri. Chotero, ndani wa iwo adzaposa kumkonda? Simoni anayankha, nati, "ndiyesa kuti iye amene anakhululukidwa zoposa."

Kodi chikhululukiro chinaika chiyani mumtima mwa wobwerekawo?

___________________________________________________________

===============================================================

14. Kukhala wokhululukidwa kunaika chikondi m'mitima yawo. Munthu amene anakhululukidwa zambiri anakondanso kwambiri. Ndipo munthu amene anakhululukidwa pang'ono anakondanso pang'ono. Simoni anali Mfarisi. Mwina iye monga mwa lamulo anali ndi timachimo tina tochepa. Koma iye sanakonde Yesu. Iye anaitanira Yesu kunyumba kukadya, koma sanapatse Yesu zinthu zimene zikanasonyeza chikondi. Yesu anachita mofatsa ndi Simoni. Iye anamuuza nthano ya obwereka aŵiri. Iye anafuna kumuonetsa kuti ngakhale machimo ake ochepawo ayenera kuti akhululukidwe.

Kodi Simoni adayenera kukhala ndi chikondi mumtima mwake pamene machimo ake akhululukidwa?

______________________________________

===============================================================

15. Simoni adayenera kukhala ndi chikondi mu mtima mwake. Chimenechi ndi chimene mkazi anali nacho. Pamene Yesu akhululukira, amatsuka mtima ndi kuulungamitsa. Yesu analandira mphatso ya mkazi. Iye anamuyamikira. Iye anakhululukira mkazi wina amene anatengedwa ali kuchita chigololo. Iye anati pita usakachimwenso. Iye sananene zimenezi kwa mkazi mnyumba ya Simoni. Iye anaonadi kuti mkaziyo walapa machimo ake kotheratu. Iye anali wokonzekera kukhala ndi moyo watsopano.

Luka 7:50:

> Ndipo Iye anati kwa mkaziyo, "chikhulupiriro chako chakupulumutsa iwe; muka ndi mtendere."

Kodi kukhala wokhululukidwa kumaika chiyani mumtima wa wokhulupirira?

___________________________________________________________

===============================================================

16. Kumaika chikondi mumtima mwa wokhulupirirayo. Chigololo sindilo tchimo lokha limene tiyenera kukhululukidwa. Mwina Simoni sanachite tchimo la chigololo. Koma kukuoneka ngati kuti iye anali wonyada ndi wodzikonda mumtima mwake. Mwina iye anali ndi mkwiyo ndi nsanje komanso machimo ena ambiri omwe anayenera kukhululukidwa.

Kuchokera m'chiphunzitso cha Yesu kwa Simoni Mfarisi ndi kwa mkazi wochimwa, kodi ife tiyenera kukhala ndi chiyani kuti tikhale wokhululukidwa?

______________________________________________

==================================================================

17. Ife tiyenera kukhala ndi chikhulupiriro kuti tikhale wokhululukidwa.

Kodi kukhala wokhululukidwa kumaika chiyani mumtima mwa wokhulupirira?

______________________________________________

==================================================================

18. Kukhala wokhululukidwa kumaika chikondi m'mitima yathu. Anthu ena amaganizira kuti ali ndi machimo ambiri omwe Mulungu sangathe kuwakhululukira. Anthu ena amati alibe machimo omwe ayenera kukhala wokhululukidwa. Phunziro lathu la lero likuonetsa kuti njira za maganizo onsewo ndi zolakwa.

Nthaŵi zina anthu samvetsetsa chimenechi. Ena amachita mantha kupempha Mulungu kuti awakhululukire. Anthu ena amaganiza kuti machimo awo sayenera kukhala wokhululukidwa.

Konzani ulaliki umene mungaulalikire kuchokera mphunziro limeneli. Pa pepala lina, lembani zinthu zikuluzikulu zimene mukanene muulaliki umenewu pa sabata ngati mungathe. Mubweretse pepala lanu ku kalasi.

==================================================================

19. Kuchokera kuchiphunzitso cha Yesu kwa Simoni Mfarisi ndi mkazi wochimwayo, kodi ife tiyenera kukhala ndi chiyani kuti tikhale wokhululukidwa?

______________________________________________

Kodi kukhala wokhululukidwa kumaika chiyani mumtima mwa wokhulupirira?

______________________________________________

==================================================================

SABATA LACHISANU NDI CHINAYI: KHRISTU APHUNZITSA ANTHU AMBIRI
TSIKU LACHIŴIRI: NTHANO YA NAMSONGOLE

1. Yesu anaphunzitsa m'njira zambiri. Taona mmene Iye anaphunzitsira mnyumba ya Simoni.

Kuchokera m'chiphunzitso cha Yesu cha kwa Simoni Mfarisi ndi mkazi wochimwayo, kodi ife tiyenera kukhala ndi chiyani kuti tikhale wokhululukidwa?

________________________________________

Kodi kukhala wokhululukidwa kumaika chiyani mumtima mwa wokhulupirira?

________________________________________

================================================================

2. Ife tiyenera kukhala ndi chikhulupiriro mmalo mofuna kukhala wokhululukidwa. Pamene ife takhululukidwa chimaikidwa chikondi mumtima mwathu.

Anthu ambiri anali kutsata Yesu kuti amve zimene Iye ali kulankhula. Nthaŵi zina Iye anali kuwaphunzitsa ndi nthano. Nthano zinali zinthu za moyo wa tsiku ndi tsiku. Zinali kuonetsa zoonadi zauzimu. Lero tiphunzira nthano ya nansongole. Yesu anaphunzitsa zinthu zambiri ndi nthano imeneyi. Ife tiphunzira zinthu ziŵiri.

(1) Potsiriza pa nthaŵi mwana wa woipayo adzaponyedwa m'moto.

(2) Ana a Mulungu adzawala monga dzuŵa mu Ufumu wa Mulungu.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Mateyu 13:24 mpaka 30. Ndipo werenganinso mmene Yesu anafotokozera bwino pa Mateyu 13:36 mpaka 43.

================================================================

3. Kodi inu mumaŵafotokozera bwanji ana anu zinthu zina zimene zili zovuta kuzimvetsetsa? Mwina inu mumapita nawo kunja ndi kukaŵaonetsa chinthu chimene mukuŵafotokozeracho. Kapena mwina inu mumaŵaonetsa chithunzi cha zomwe muli kunenazo. Ngati inu simuchita zimenezi mukhoza kungoŵauza nthano. Zimenezi ndi zimene Yesu anachita. Iye anafuna kufotokoza kuti kuli anthu amitundu iŵiri m'dziko lapansi.

Mateyu 13:24-25:

Fanizo lina Iye anaŵafotokozera iwo, nanena, Ufumu wa Kumwamva ufanizidwa ndi munthu, amene anafesa mbewu zabwino m'munda mwake; koma mmene anthu analinkugona, mdani wake anadza, nafesa namsongole pakati pa tirigu, nachokapo.

Kodi inu mukuganiza kuti Yesu anali kunena za anthu amitundu iŵiri yotani amene anafanizidwa ndi mbewu yabwino ndi namsongole?

(1) ____________________ (2) ____________________

==================================================================

4. Kapena mwalemba "anthu abwino" ndi "anthu oipa." Kapena mwalemba kuti "okhulupirira" ndi "osakhulupirira" Zimenezi ndi zolondola. Yesu anauza anthu nthano imeneyi kuti amvetsetse choonadi cha Uzimu. Namsongole akhoza kukhala vuto lalikulu m'munda. Akhoza kutsamwitsa mbewu kuti zisakule. Akuphunzira anapempha Yesu kuti afotokozere bwino nthanoyi.

Mateyu 13:37-28:

Ndipo Iye anayankha nati, wofesa mbewu yabwino ndiye mwana wa munthu; ndipo munda ndiwo dziko lapansi; ndi mbewu yabwino ndiyo ana a Ufumuwo; ndi namsongole ndiye ana a woipayo.

Kodi ndi mtundu uti wa anthu amene ali mbewu yabwino m'nthano imeneyi?

____________________________________________________________

==================================================================

5. Iwo ndi ana a Ufumuwo. Chimenechi chimatanthauza kuti ndi ana Mulungu. Iwo analandira Khristu.

Mateyu 13:38-39:

Ndipo munda ndiwo dziko lapansi; ndi mbewu yabwino ndiwo ana a Ufumuwo; ndi namsongole ndiye ana a woipayo; ndipo mdani amene anafesa uwu, ndiye mdierekezi.

Kodi ndi ndani anafesa namsongole yemwe ali monga anthu oipa a dziko lapansi?

____________________________________________

==================================================================

6. Amene anafesa ndi Satana. Iye ndi mtsogoleri wa anthu oipa a m'dziko lapansi.

Mateyu 13:28-29:

> Ndipo iye ananena kwa iwo, munthu mdani wanga wachichita ichi. Ndipo anyamata anati kwa Iye, kodi mufuna tsopano kuti timuke, tikasonkhanitse uyo pamodzi? Koma Iye anati, iyai, kuti kapena mmene mukasonkhanitse namsongoleyo mungazulirenso tirigu pamodzi naye?

Kuchokera m'ndime iyi, kodi ndi chifukwa chiyani mwini mundayo sanafune kuti namsongoleyo azulidwe ndi kukamutentha nthaŵi yomweyo?

_ __________________________________________________________

==========================================================================

7. Iye anali kuopa kuti mwina pozula mbewu zabwinonso akhoza kuzuka. Mulungu amafuna kuti anthu abwino ndi oipa azikhalira pamodzi m'dziko. Koma tsiku lina wosakhulupirira adzalangidwa.

Mateyu 13:30:

> Kazilekeni zonse ziŵiri, zikulire pamodzi kufikira pakututa; ndimo mnyengo yakututa ndidzauza akututawo, muyambe kusonkhanitsa namsongole, mummange uyu mitolo kukamutentha, koma musonkhanitse tirigu m'nkhokwe yanga...ndi kututa ndicho chimaliziro cha nthaŵi ya pansi pano.

Kodi ndi liti limene mwana woipayo adzaponyedwe pamoto?

____________________________________________________________

==========================================================================

8. Pamenepa padzakhala pachimaliziro cha nthaŵi ya pansi pano. Mulungu amaŵaleka kuti apitirizebe tsopano. Nthaŵi zina ife timayang'ana kwa anthu amene samvera Mulungu. Ife timadziŵa kuti ali kuchita zinthu zolakwa. Ife timadziŵa kuti iwo ndi ana a Satana. Ife timadabwa kuti iwo amapitiririrabe kukhala m'moyo wa uchimo. Mulungu samaŵalanga iwo. Iye amaŵalekerera kuti azingopitiririrabe. Koma nthaŵi ikudza imene mwana wa woipayo adzalangidwa.

Kodi ndi anthu ati amene ali ofanana ndi namsongole ndipo iwo adzatenthedwa pakutha pa nthaŵi yake?

_____________________________________

9. Amenewo ndi ana a woipayo.

Mateyu 13:40-42:

> Ndipo monga namsongole asonkhanitsidwa pamodzi, natenthedwa pamoto, motero mudzakhala m'chimaliziro cha nthaŵi ya pansi pano. Mwana wa munthu adzatuma angelo ake, ndipo iwo adzasonkhanitsa pamodzi, ndi kuchotsa mu Ufumu wake zokhumudwitsa zonse, ndi anthu akuchita kusayeruzika ndipo adzaŵataya iwo mng'anjo ya moto.

Kodi chidzaoneka ndi chiyani kwa namsongole kapena ana a woipayo pa nthaŵi ya chimaliziro? ________________________________________

________________________________________________________________

================================================================

10. Iwo adzaponyedwa m'moto. Imeneyi idzakhala nthaŵi ya chimaliziro. Nthaŵi zina zimenezi zidzachitikanso kwa mbewu yabwino kapena tirigu.

Mateyu 13:41-43:

> Mwana wa munthu adzatuma angelo ake, ndipo iwo adzasonkhanitsa pamodzi, ndi kuchotsa zonse, ndi anthu akuchita kusayeruzika, ndipo adzaŵataya iwo mnng'anjo ya moto; kumeneko kudzakhala kulira ndi kukukuta mano. Pomwepo wolungama adzawalitsa monga dzuŵa, mu Ufumu wa Atate wawo.

Kodi ndi ndani amene adzasonkhanitsidwe pamodzi ndi kudzawala mu Ufumu wa Mulungu? ________________________________________

================================================================

11. Amenewo ndi wolungama kapena ana amu Ufumuwo. Ndani anafuna kuononga mbewu m'munda. Satana amafuna kuononga ntchito ya Mulungu ndi ya ana a Mulungu. Koma mdani sanakhoze kuononga mbewu. Ndipo Satana sangathe kuononga Mkhristu. Akhristu oonadi adzakula mwa mphamvu. Iwo adzapitiriza kutsatira Yesu ngakhale kuti Satana ali kukhala pafupi ndi iwo.

Kuchokera m'nthano ya namsongole, kodi chidzaoneka ndi chiyani kwa namsongole, amene ali ana a woipayo? ______________________

12. Iwo adzaponyedwa pamoto. Koma mbewu zabwino zidzaikidwa mnyumba yosungiramo. Taonaninso mmene Yesu ali kufotokozera mbali ya nthano imeneyi.

Mateyu 13:43:
> Pomwepo olungamawo adzawalitsa monga dzuŵa, mu Ufumu wa Atate wawo. Amene ali ndi makutu amve.

Pa chimaliziro, kodi ndi ndani amene adzawale monga dzuwa mu ufumu wa Atate wawo?

______________________________

==================================================================

13. Amenewo ndi anthu olungama kapena ana a Ufumuwo. Iwo adzawala monga dzuŵa . Mulungu mu nthaŵi zakalekale lomwe anamuonetsa mneneri Danieli.

Danieli 12:3:
> Ndipo aphunzitsi adzaŵala ngati kunyezimira kwa thambo ndi iwo otembenuza ambiri atsate chilungamo ngati nyenyezi ku nthaŵi za nthaŵi.

Kodi ndi liti limene ana a Ufumuwo adzawale monga dzuŵa mu Ufumu wa Mulungu?

______________________________

==================================================================

14. Zimenezi zidzakhala pa chimaliziro cha nthaŵi. Mulungu samachotseratu anthu oipa tsopano. Iye ali kuŵapatsa mwayi wakuti alape. Satana adzayesetsa kugwiritsa ntchito anthu ameneŵa kuti aononge ana a Ufumu. Koma iwo sadzatha kuchita zimenezi.

2 Petro 2:9:
> Ambuye adziŵa kupulumutsa opembedza poyesedwa iwo, ndi kusunga osalungama kufikira tsiku loweruza akalangidwe.

Pa chimaliziro cha nthaŵi, kodi chidzaoneka ndi chiyani kwa mbewu yabwino amene ali ana a Mulungu?

______________________________

______________________________